


# *NDIPO KUYAMBIRA*

## *NTHAWI IMENEYO*

 Ndithudi nchabwino kubwereranso ndi kudzamumva m'bale, m'busa, akupereka umboni wa chisomo cha Mulungu, ndi mtsikana wake wamng'ono. Izo ndi chimodzimodzi ngati Ambuye Yesu, kuchita zinthu monga zimenezo. Ndithudi ndi choncho.

<sup>2</sup> Tsopano, ife tiri okondwa kwambiri, usikuuno, kukhala nafe ife, mmodzi wa alendo athu kuno ku, monga ife timazitchulira izo, msonkhano wa pemphero pa usiku wa Chaka Chatsopano, mzanga wabwino wa ine, M'bale Ernie Fandler, mmodzi wa owatembenezira kwa Ambuye Yesu Khristu, chikho cha chisomo. Kwawo kochokera ku Switzerland, ndi kumene iye anachokerako. Ndipo ine ndikukhulupirira, m'bale yemwe ali ndi iyeyo pamenepo, amene iwo akukhala ku Shawano tsopano, ochokera ku German, M'bale Waters. Ndife okondwa kukhala nawo iwo usikuuno.

<sup>3</sup> Ndiye ife tiri, nayenso, pano usikuuno, a—m'bale wofunika wa chikhulupirochi, South Africa, M'bale David duPlessis. Ndife okondwa kukhala naye iye, nayenso. Ndipo ife tiri, David ndi ine, ti—tikuyembekezera, tikupemphera, Ambuye, kuti atipatse ife ntchito ina yopambana pamodzi, chaka chikubwerachi, mu Afrika ndi magawo osiyanasiyana a dziko. M'bale David wabwera kuno tsopano kuti tidzakambirane, ndi kudzazipempherera izo, pakati pa tsopano ndi Lolemba, kuti tigamule kuti ndi liti ndi kuti, mu—ku Afrika, ndi magawo osiyanasiyana a dziko koti tipiteko. Monga, M'bale David wakhala ali ndi ofesi yayikulu kwambiri ndi a Pentecostal World Convention, ndiponso ndi wodziwika-bwino ndi atosogoleri ambiri aakulu azipembedzo pa dziko lonse. Ndipo wakhala ali ndi chikoka chowalimbikitsa ndi kuwapangitsa, nthawi yomwe takhalira limodzi mpaka pano, kuti tithandizire kulibweretsa Thupi la Yesu Khristu pamodzi, la zipembedzo zonse za chikhulupiriro. Mosalabadira mpingo umene (iwo) ali nawo, kapena chimene (iwo) dzina limene iwo amatchulidwa nalo. Ndi icho, Mpingo, Umene Khristu anauffera.

<sup>4</sup> Ndipo kawirikawiri ine ndimaganiza za zimenezo. Ndinkakonda kuthandizira kukusa ng'ombe, nthawi zambiri, uko Kumadzulo. Ife timakhoza kupitako, M'bale David, ndi kukakhala uko kumene iwo amazidusitsa ng'ombezo ku mpanda wa kulowerera, uko mpaka ku mapiri, kuti akazidyetse izo pa . . .kuzisiya izo kuti zizidya pa msipu, a . . .

wa mnkhalango. Pamene, udzu wa nsenjere ukukula mmusi, udzu wa nsenjere wakuthengo. Kenako iwo amadula nsenjerezo, ndi kumakazidyetsa ng'ombezo kudutsa—kudutsa nthawi ya chisanu, pamene kumakhala nkuntho wachisanu wawukulu, ku mapiriko.

<sup>5</sup> Ndipo ndinkakonda kukhala pamenepo pa chishalo ndi kumawona woyang'anira zinyama akuzidutsitsa ng'ombe zimenezo; ndipo kodyetsera ziweto kulikonse, mmusi, amene amakwanitsa tani ya msipu. Ngati iwo akwanitsa matani fifite a msipu, zimenezo zimatanthauza kuti iwo amakhoza kuziikamo ng'ombe fifite. Ngati iwo akwanitsa matani sauzande a msipu, ng'ombe sauzande zimakhoza kudutsamo. Munthu aliyense, atanyamula mtundu pa ngombe zake. Iwo amayanganyitsitsa mitundu, ndithudi, kodyetsera ziweto kosiyanasiyana, kuwopa kuti zisasakanizikane. Ndiyeno pamene a . . .

<sup>6</sup> Woyang'anira zinyama, iye analibe chidwi kwambiri ndi mtundu umene umadutsa, chifukwa pamakhala mitundu yosiyanasiyana. Koma panali chinthu chimodzi chimene kwenikweni iye amachiyang'ana, chimenecho chimakhala chizindikiritso cha mtundu wa magazi. Izo zimayenera kukhala za Hereford zolembetsedwa, kapena izo sizimadutsa pa chipatacho. Iwo amazibweza izo. Mukuona?

<sup>7</sup> Ndipo ine ndikuganiza kuti umo ndi mmene ziti zidzakhali pa Chiweruzo. Izo sizidzakhala kuti ndi mtundu wanji umene ife tavalala, koma ngati chizindikiritso cha mtundu wa Magazi chiri pamenepo. Chimenecho ndicho chinthucho—chimene chiti chidzafunidwe, chizindikiritso cha mtundu wa Magazi.

Ndipo ndine wokondwa kwambiri kukhala ndi M'bale David limodzi nafe.

<sup>8</sup> Ndipo ine ndinamuwona M'bale Estle Beeler anali pano kamphindi kapitako. Ine ndinamuwona iye akudzuka kumbuyo uko, kuchokera kwinakwake. Ndi atumiki ena amene timafuna kuti tiwamve, usikuuno. Ndipo, ndiye, ndipo ine ndikuganiza M'bale Ruddell ndi iwo akhala akubwera, chifukwa iwo akhala mpaka pakati pa usiku.

<sup>9</sup> Komabe, M'bale David sangakhale mpaka pakati pa usiku. Iye ndi mwamuna wofunidwa kwambiri, konsekonse. Ndipo mwamsanga M'bale Rodgers atangomva kuti iye ali kuno, bwanji, iye atumiza ndipo akakhala naye iye kumeneko mma teni. Chotero izo zikutanthauza kuti iye akhala akuchoka kuno, posakhalitsapa, kuti apite uko kummwera mu Louisville.

<sup>10</sup> Ndipo ine ndinaganiza kuti icho chingakhale chabwino, ngati zingakhale zabwino ndi M'bale David, ngati—ngati ife tingamubweretse iye kuti adzayankhule chimene chiri pa mtima wake, kutilalikirira ife, kuchita chirichonse chimene Ambuye angakupatseni. Ife tonse tikufuna kumumva M'bale David duPlessis, wochokera ku South Africa.

<sup>11</sup> Mundilole ine ndinene ichi. Kuti, pamene ine ndinali, uko ku Afrika, mu msonkhano wanga waukulu wokopa anthu umene Ambuye anatipatsa ife kumeneko, m'bale wake anali wotanthauzira wanga, M'bale Justus. Ine ndikukhulupirira dzina lake ndi M'bale Justus. Ndi banja labwino kwenikweni la anthu, a duPlessis apachibale onse awa. Ine ndikuganiza pali . . . ine ndikuganiza kuti iwo onse ndi atumiki, monga mmene ine ndikudziwira, ndipo mwinamwake abambo, nawonso, kuti anali mtumiki. Ndipo iwo ndi ochokera ku banja labwino la anthu. Ndipo M'bale David amanyamula dzina lalikulu pakati pa mipingo yonse ndi zipembedzo kuzungulira dziko.

<sup>12</sup> Ndipo M'bale David, ine ndikufuna kuti inu mubwere tsopano ndipo mudzatiyankhulire ife, kapena chirichonse chimene Mulungu waika pa mtima wanu kuti munene. Bwerani kuntunda kuno. Ndipo ndine wokondwa kwambiri kukuwonetsani kwa mpingo wanga, usikuuno. Awa ndi M'bale Orman Neville, abusa athu. Ndipo kwa mpingo, uyu ndi mmodzi wa azimzanga ofunika, ndi—ndi ankhondo amzanga mu utumiki wa Mulungu, M'bale David duPlessis waku South Africa. Mulungu akudalitseni inu, M'bale David.

<sup>13</sup> [M'bale David duPlessis akuyankhula. Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . yankhulani. Ameni. Ife tonse tatero. M'bale David, mubwerere mofulumira ndipo mudzakhale nafenso. Izo ndi zabwino kwambiri. Ndithudi ndife okondwa.

<sup>14</sup> M'bale David ananena zinthu zina pamenepo, ine ndimangokhumba ndikanakhala ndi cholemba changa, ine ndikanazilemba izo. Koma ine nthawizonse ndizikumbukira “adzukulu aamuna; zidzukulu.”

<sup>15</sup> Chabwino, ife ndithudi tikuyamikira kudzatichezera kwa m'bale wathu. Ndipo iye ali . . . anali . . . wolumikizana ndi okhulupirira a World Conference of Pentecost, ndipo mwamuna wamphamvu mu mzere wa ntchito yake kudutsa dziko lonse. Ndipo ndife a mwayi, usikuuno, kukhala ndi M'bale David kuti anabwera kudzayankhula nafe pa usiku wa Chaka Chatsopano uwu. Ndipo inu mukhoza kuwona chimene amuna amphamvu amaganiza za Ambuye wathu, amaganiza za wantchito Wake wamphamvu.

<sup>16</sup> Tsopano ine ndikukhulupirira kuti, mawa, pokhala Chaka Chatsopano, kwangotsala maora pang'ono tsopano. Ndipo ine ndikuyenera kudzachoka molawirira mmawa, chotero ine ndinaganiza kuti ine ndingoyankhula pang'ono, ngati izo ziri bwino ndi M'bale Neville. [M'bale Neville akuti, “Inde. Ameni.”—Mkonzi.] M'bale Beeler, ndi atumiki enawo pano. Sinditenga nthawi yambiri. Ndipo ine ndikuganiza, ngati ife titanena “Ameni,” ndi kumapita kwathu, iwo ukhoza kukhala uthenga wopambana. Ndipo ife tikhoza kukhala othokoza kwa Ambuye pa chimene ife tiri nacho pano, usikuuno.

<sup>17</sup> Ndipo tsopano, koma uno pokhala usiku wa Chaka Chatsopano, ife timangosalatsana wina ndi mzake, mwa Ufumu wa Mulungu, kulalikira, mpaka kufika mu Chaka Chatsopano. Ndipo ine ndiri. . . ndinadzuka mmawa, molawirira kwenikweni, kusanache. Ndipo ine si wachichepere monga David. Mwinamwake ine. . . Mwinamwake ine sindidzimverera kuchepa monga iye amadzimverera. Iye ndi. . . Ndithudi, David ndi wamng'ono—wamkulu pang'ono kundiposa ine. Ine ndikuganiza iye ndi wamkulu ndi zaka seveni kapena eyiti, mwinamwake teni. Koma ndithudi iye ndi wamoto kwa Mulungu, wayenda mailosi fifite sauzande chaka chino, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Ali pa msewu tsopano kuti akalalikire kwa M'bale Rodgers, ndipo mawa akakhala ndi ena, kwinakwakenso, ndi kwinakwakenso, ndi kwinakwakenso, ndipo kudzabwereranso kuno Lolemba. Ndipo ine ndikuyenera kukumana naye iye kuti tipange dongosolo la ulendo wa dzikolonse umene ukubwera tsopano.

<sup>18</sup> Ndipo ife tikuyenera kukakhala mu Afrika, ine ndinamvetsedwa masana ano, mu Malichi, uyu—Malichi akubwera uyu. Ine ndikuyenera kukumana ndi Clayton Sondmore, wochokera ku Full Gospel Christian Business Men, sabata ino, kapena sabata ikubwerayi, gawo loyamba la iyo, ndi kukonza madongosolo aku Jamaica, Haiti. Ine ndipitako sabata ya mawa ku Kentucky, kapena kudzatsika mpaka ku Georgia, kukakhala ndi misonkhano imeneyo uko. Kudzabwereranso ndi kudzabwera ku Kentucky, usiku kuno, ndi usiku kumeneko, kuigwira mipingo imeneyi. Ndipo nkudzabwereranso molunjika kuno tikuchokera kumeneko, ndipo nkudzapita ku—ku—ku Atlantic City, kuyambira pa 27, kudutsa pa 30, ndi kudzachoka kumeneko mmawa wa pa 1, ndi kukayambira mu—mu Kingston, Jamaica, ku— . . . bwalo la mjaha, usiku umenewo, ku msonkhano wa masiku teni kumeneko. Ndipo kuchokera kumeneko, kenako kwa achi Haiti, ndi kulikonseko. Ife sitikudziwa kuti tidzapita kuti tikadzachoka kumeneko, basi mmene Ambuye ati adzatitsogolere ife.

<sup>19</sup> Tsopano, zonsezi zikukonzedwa. Mukuona? Ine sindinavomerezebe. David ali pano, Clayt akubwera. Gordon, M'bale Gordon Lindsay akubwerera, South America. Ndipo—ndipo ena onsewo, a Christian Business Men Achimerika oyankhula chi Latin. Ndipo M'bale David ndi wa ku Switzerland, Germany, mpaka mmusi. Koma ife sitikudziwabe. Inu mupitirize kumapemphera. Ine sindikufuna kupita kulikonse mpaka Mulungu atanena kuti ndipite, ndizo mwakupambana kwa kudziwa kwanga. Chotero, ngati ine ndimverera kutsogozedwa kuti ndipite, ndiye ndikatsika ndege, ine. . . Ndipo ziribe kanthu kuti kuli zonditsutsa zotani, ine ndimakhoza kunena kuti, “Ine ndabwera mu Dzina la Ambuye Yesu.”

<sup>20</sup> Ine ndinali wothokoza chifukwa cha David, ubwenzi umene ife takhala tiri nawo, chifukwa munthuyo ndi munthu wofunika kwambiri, koma iye—iye—iye ndithudi amakhulupirira utumiki uwu wa Ambuye. Iye ndithudi amatero. Ndipo—ndipo maina athu akhala akuyendera limodzi mu dziko lonse tsopano, M'bale David ndi ine.

<sup>21</sup> Ndipo ndine wokondwa kwambiri kukhala pachiyanjano ndi munthu ngati ameneyo. Koma, abwenzi, ine ndikuyamikira zimenezo. Koma chinthu chachikulu kwambiri chimene ine ndingachiganizire kuti ndingayanjane nacho ndi Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, Mmodzi wamkulu ameneyo.

<sup>22</sup> Tsopano, M'bale Neville ndi ena a iwo akhala akuyankhula mu mphindi pang'ono, koma ine ndikufuna kuti ndiwerenge chinachake chaching'ono kuchokera mu Lemba tsopano.

<sup>23</sup> Ndipo ndi zabwino, ine ndikuganiza, pa usiku wa Chaka Chatsopano, kuwona alaliki osiyanasiyana, ndi mmene iwo amafikira pa mutu, ndi zimene iwo amanena, ndi zina zotero. Ndipo mwamuna aliyense amakhala ndi njira yake yake ya kalalikidwe. Inu mukudziwa, Mulungu sanatipange ife tonse kukhala ofanana. Iye anatipanga ife osiyanasiyana. Iye anatipanga ife osiyanasiyana mu thunthu lathu. Iye analipanga dziko losiyana, ndi mapiri aakulu, timapiri tating'ono, mathengo, zipululu, maluwa aakulu oyera, maluwa a buluu, ndi mitundu yonse yosiyanasiyana. Iye amangotipanga ife kukhala osiyanasiyana. Ndizo zonse. Iye amapanga mutu wofiira, ndi mitu yakuda, mitu yabulauni, mutu woyera; onepa, owonda, aatali, oh, chirichonsecho. Mukuona? Iye basi— Iye amangotipanga ife kukhala osiyanasiyana. Mulungu ndi Mulungu wakasinthasintho. Ndipo ine ndimazikonda zimenezo. Inu simumatero? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Koma basi chinthu chomwecho nthawi zonse? Mai! Mai! Ine ndimazikonda zimenezo.

<sup>24</sup> Chotero tiyeni ife tsopano titembenezire ku Malemba athu, ku Bukhu la Mateyu Woyera, Uthenga wa Mateyu Woyera, kuyambira ndi...Ndi ndime ya 4, ine ndikufuna kuti ndiwerenge pa...tiwerenge mutu, Ambuye atithandize ife. Mateyu Woyera, mutu wa 4.

Ine ndikukhulupirira, ife tisanawerenge, tiyeni tipemphere.

<sup>25</sup> Atate Akumwamba Achisomo, kenanso ndi mitima yoyamikira ife tikuyandikira chaka chatsopano ichi. Ndipo ife tikukuyandikirani Inu ndipo tikubweretsa kwa Inu nkhawa zathu zonse zammbuyo, ndipo tikupemphera kuti Inu mukaziike izo mu nyanja ya kuiwala, ndipo musadzakumbukirensa machimo athu pa ife kenanso. Ndipo mulole kuti tisangofufuza umunthu wathu wauzimu, koma mwathu...mulole tifufuze chiyanjano chathu ndi Inu. Ndipo tikhululukireni ife machimo athu onse. Ndipo tikupemphera kuti Mzimu Wanu uchite nafe

ife usikuuno. Ndipo ngati pangakhale chinthu chodetsedwa cha ife, Ambuye, chitengereni icho kutali monga kummawa kwatalikirana ndi kumadzulo. Mukachiponyere icho mu nyanja ya kuiwala, kuti musadzakumbukirensa icho pa ife, kuti ife tithe kulowa mchaka chatsopano ichi, oyera, otsukidwa ndi Magazi a Mwanawankhosa, ndipo tikakhale okonzeka.

<sup>26</sup> Mulole 1960 uyu akhale chaka chopambana chimene ife tinayamba takutumikirani Inu. Mutipatse ife zopitirira, zochulukana. Misonkhano yonse iyi imene ikuchitika, Ambuye, imene ife tikuiganizira ndi M'bale duPlessis, ndi kuzungulira dziko, kupita mu Asia, ndipo mpaka ku Europe, ndi konse—konse konse. Ambuye, mulole chikhale chifuniro Chanu ndi Mphamvu Yanu imene iti ititsogolere ife ku zinthu izi. Ndipo ngati pa nthawi iliyonse tingadzachoke pa njira Yanu Yaumulungu yodzodzedwa, mulole Mzimu Woyera udzaike chotchinga panjirapo ndipo udzatiimitse ife, Ambuye, ndipo udzatiabwezere ife ku malo oyenera. Perekani izi.

<sup>27</sup> Mudalitse mpingo waung'ono uno, Ambuye. Pafupifupi, kuyandikira zaka sate, ine ndikuganiza, iwo ukuima pano tsopano, ngati chikumbutso cha chisomo cha Mulungu, kwa anthu odzichepetsa. Ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mumudalitse M'bale Neville, m'busa. Mudalitse mpingo wonse. Mudalitse matrastii, madikoni, wotsogolera nyimbo, wa limba, ndi osonkhana onse, wina aliyense, aphunzitsi a Sande sukulu, aliyenseyo. Ambuye, mulole ife tikathe kukula mchaka chino mu chisomo cha Mulungu. Ndipo mulole mamembala athu akakule kukhala ziwerengero zazikulu, ndi—ndi chisomo chochulukana Chanu, kuti, zoposa izi zakhala ziri mu zaka zapitazi. Perekani izi, Atate.

<sup>28</sup> Tsopano tithandizeni ife pamene ife tikuyandikira mutu uwu umene ife tikukonzekera kuti tiwerenge, Mawu Anu. Ndipo Inu nokha, Ambuye, mukhoza kutanthauzira ndipo ife tikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa ife, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

<sup>29</sup> Ine ndilengeza posakhalitsapa chimene ine ndasankha kukhala mutu kwa mphindi pang'ono zotsatirazi. Iwo ukupezeka mu Lemba apa, ndipo ine ndiwerenga iwo. Iwo ukutchedwa, ine ndikufuna kuwutcha iwo ichi, “kuyambira nthawi imeneyo.”

<sup>30</sup> Ine sindimaziganizira, ine ndinanena usiku wina, ine sindimayembekezera kuti ine ndibwera kuno, chifukwa chakuti kummero kwanga kumawotcha. Ndipo mkazi wanga ananena kwa ine dzulo, kapena dzana, iye anati, “Ndiye ine ndikuganiza kuti iwe sukhalala ukupita ku tchalitchi.”

<sup>31</sup> Ndipo ine ndinati, “Wokonedwa, ine sindikuganiza chomwecho. Kukhosi kwanga kukupweteka kwambiri ndi kuwotcha.”

<sup>32</sup> Ndipo kenako, usiku womwewo, pamene ine ndinakhala pansi ndikutenga Lemba, ine ndinakumanizana nacho Ichi.

<sup>33</sup> M'bale Sothmann anadzabwera. Iye anati, "Kodi inu mukhala mukupita ku tchalitchi mawa usiku?"

Ine ndinati, "Eya. Ine ndidzakakhala komweko."

<sup>34</sup> Ndipo Meda anadzayang'ana mopotolokera kwa ine, ndipo iye anati, "Ine sindimakumvetsa iwe."

Ine ndinati, "Ine sindimayembekeza kuti iwe udzitero, mwaona," ine ndinati, "kapena wina aliyenseyo."

<sup>35</sup> Palibe aliyense amene amatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu amene angamvetsedwe konse.

<sup>36</sup> Ambuye wathu, iwo sanathe kumumvetsa Iye. Iye amawoneka ngati Iye amayankhula zotere, miniti imodzi; ndi mwanjira ina, miniti inayo. Ndipo pena Iye amayankhula za chinachake. Nthawizina amakhala ali Yesu akuyankhula, nthawi zinazo amakhala ali Mulungu akuyankhula. Inu mukuona? Ngakhale ophunzira ananena pamenepo, potsiriza, anati, "Taonani, tsopano Inu mwayankhula momveka bwino. Tsopano ife tikumvetsa." Mukuona?

<sup>37</sup> Ndipo Yesu anati, "Kodi inu mu- . . . Ndipo kodi inu tsopano mukukhulupirira?" Mwaona, zitatha zimenezo.

<sup>38</sup> Iwe basi sungathe kuchita izo, chifukwa iwe ukutsogozedwa ndi Mzimu. Ndipo iwe ukayamba kuchita chinachake, iwe umadzapeza kuti, inu mwaona, ndiwe. . . Mulungu akufuna akakugwiritse iwe ntchito kwinakwake. Iwe umayenera usiye *apa* ndi kupita *apa*, basi kumangotsogozedwa ndi Mzimu. Iwo amakhala osamvetsetseka, anthu achilendo amene amakhala ndi moyo umene umayenera kudzipereka kwa Mulungu.

<sup>39</sup> Ndiyeno ine nthawizonse ndimanena izi, "Ine ndichita ichi ngati Ambuye alola." Mukuona? Ngati ine ndimulonjeza aliyense, "Ine ndichita icho ngati Ambuye alola." Mukuona? Ndipo chotero, ndiye, ngati icho si chifuniro cha Ambuye, ine ndimakhala. . . ine ndidzayankhula pa Uthenga uwu ngati Ambuye alola. Iye akhoza kunditana ine, ndiri pakati pa Uthenga uwu, kuti ndizinyamuka ndizipita ku California. Ine ndingasiye chirichonse kumbali ndi kunyamuka kumapita ku California, mwamphamvu monga mmene ine ndingathere.

<sup>40</sup> Ndipo ine ndimafuna ndizikhala monga chomwecho. Ine sindimafuna kanthu kalikonse kuti kazindimangilira ine pansi. Ine sindifuna chinachake chachikulu kapena chimzake, kumene kuli mamilioni a madolla, ndipo iwe uzilandira ndalama zochuluka chomwechi, tsiku ndi tsiku, kuti zindimangilire ine pansi. Ine ndimafuna kumakhala, kumene, pamene Mulungu akanena kuti, "Ine ndikufuna iwe upite kumusi kuno kwa anthu awa. Alipo faifi okha a iwo. Koma upite kumeneko, ndipo ukakhale kumeneko mpaka Ine nditakuuza iwe kuti

uchokeko.” Ine ndingafune kupita kumeneko. Sindimakhala ndi chondimangirira chirichonse, basi. . . ndipo ngati Iye akufuna kuti ine ndipite kutsidya kwa nyanja.

<sup>41</sup> Tsopano ndi izi apa, zangotchulidwa kumene, kupita ku Germany, kapena ku—ku Afrika. Ndipo mkazi wina wa mamilioni, basi nthawi imene Mzimu Woyera unadzaika pa ine kuti ndipite ku Afrika, iye anati, “Ine ndithandizira ulendowo ndipo ndilipira chirichonse cha iwo.” Mukuona? Ndizo zonse. Ine nchifukwa chiyani kuti ndizidandaula za ndalama ndi zinthu, pamene Atate anga ali ndi zonse za izo? Mukuona? Iwo akhoza kungoyankhula kwa mwamuna wolemera uyu, kapena mwamuna wolemera uyo, kapena anthu awa, kapena anthu awo, ndipo palibepo chifukwa choti ine ndizikhalira kudandaula za izo. Mukuona? Mulungu amangosamalira zonsezo.

<sup>42</sup> M’bale Roy, ndiyo njira yokhalira moyo. Kungomusiya Iye azisamalira izo. Izo ndi zabwino kwambiri.

<sup>43</sup> Tsopano tiyeni titembenezire mu Malemba athu, ku mutu wa 4. Ndipo tiyeni tiyambire ku—kuwerenga, pafupifupi ndime ya 12 ya mutu 4 wa Uthenga molingana ndi Mateyu Woyera.

*Tsopano pamene Yesu anali ata. . . Ndipo tsopano pamene Yesu anamva kuti Yohane waikidwa mu ndende, iye ananyamuka kupita ku Galileya;*

*. . . kuchoka ku Nazareti, iye anafika ndipo anadzakhala mu Kaperna, amene ali pa gombe la nyanja, ku malire a Zabuloni ku Nefitali:*

*Kuti chikakwaniritsidwe chimene chinanenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti,*

*Dziko la Zabuloni, ndi dziko la Nefitali, njira ya ku nyanja, kudutsa Yordani, Galileya wa Amitundu;*

*Anthu amene anakhala mu mdima anawona kuwala kwakukuru; ndipo kwa iwo amene anakhala mu madera a mthunzi wa imfa kuwala kunawatulukira.*

*Kuyambira nthawi imeneyo Yesu anayamba kulalikirira, ndi kuti, Lapani: pakuti ufumu wa kumwamba wayandikirira.*

<sup>44</sup> Ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro: *Ndipo Kuyambira Nthawi Imeneyo.* Inu mukudziwa, ngati anthu, ife tonse timaganizira zinthu kuchokera pa nthawi inayake. Chinthu chakuti-ndi-chakuti chinachitika, ndipo kuyambira nthawi imeneyo. Ndipo tsopano, nthawi zambiri, inu mukakumana ndi bambo wokalamba kapena mayi wokalamba, ndipo iwo amakonda kuloza ku nthawi imene chinachake chinachitika, kuti iwo akhoza mosiyanitsa kuchiloza icho ndi kuti, “Zinali pa nthawi imeneyo.”

<sup>45</sup> Tsopano, ine ndikuganiza kuti pafupifupi tonse a ife pano, usikuuno, tikhoza kukumbukira membala, kukumbukira zinthu



zina zimene zinadzachitika pa nthawi inayake. Kuyambira nthawi imeneyo, chinachake chinasintha. Chinthu *chakuti-ndi-chakuti*, chinachitika pa nthawi imeneyo. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, izo zinasintha. Ndipo ndi chinthu chabwino kuti ife tikhoza. Ndipo zina za zikumbutso zimenezo, za zinthu zimene ife timaziganizira, ndi zinthu zoyenera zimene zinasintha. Ndipo pali zinthu zina zimene ziri zosayenera kuziganizira.

<sup>46</sup> Mwa chitsanzo, ngati mkazi wambiri-yoipa, iye akanati, “Panali nthawi imene ine ndinali mtsikana wabwino, worungama, wakhalidwe. Ndipo usiku wina, kapena malo enaake, chinthu chinachake chinadzachitika.” Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye wakhala ali panjira yolakwika. Moyo wake wawonongedwa ndi tchimo, ndi zakuda ndi mdima, ndipo chiweruzo chokha nchimene chikumudikirira iye. Koma iye akhoza kukumbukira, kuyambira nthawi imeneyo, izo zinachitika pamene iye anatenga njira yolakwika.

<sup>47</sup> A—bambo woledzera, usikuuno, amene ali pa misewu, amene akuyesetsa kumwa kuti achotse nkhowa zake. Inu mukhoza kumutola iye. Monga ine ndinali uko ku bowery kuno, nthawi ina kale, mu New York, pachirikati penipeni pa anthu oledzera. Ine ndinkayenda ndi mtumiki winawake. Ndipo pamenepo panagona mwamuna, oh, kunangokhala amuna ambiri, osawopsya, wopanda thandizo, atagona pamenepo kutsogolo kwa zovala zawo konse kutanyowa, ndi—ndi ndevu zawo ziri pa nkhope pawo ponse, ndipo basi ali mu chikhalidwe choipa. Ndipo iwo anali osawopsya ndithudi.

<sup>48</sup> Ndipo mtumiki uyu anati, “Mzutseni mmodziyo, ndipo mungomufunsa iye.”

<sup>49</sup> Ndipo ine ndinapita kwa bambo uyu amene anali atagona ali ndi mwendo umodzi pa bampala ya galimoto, ndipo mutu wake utagona pansu mu msewu, ndipo kuti iye amalephera ku—ku—kuti apite nthawi zina, ku malo odzithandizira. Oh, iye anali basi mu chikhalidwe choipa. Ndipo ine ndinamugwira iye, ndipo ine ndinati, “Kodi iwe ungate kuyankhula?” Ndipo iye samandiyanika ine.

<sup>50</sup> Chotero mtumikiyo anatsika. Iye amadziwa mochuluka mmene angachitire naye iye. Ndipo iye anamufunsa iye, “Iwe ndi ndani?”

<sup>51</sup> Ndipo potsiriza iye anamudzutsa iye mokwanira, mpaka iye anati, “Ngati iwe ungandigulire ine chakumwa!” Ndipo tinadzapeza kuti, iye amatha kuloza chala chake ku banki imene iye anali purezidenti wake.

<sup>52</sup> “Chabwino,” iye anati, “ife ndi alaliki. Kodi iwe ungandiuze ine chimene chinachitika?”

“Ngati inu mungandilonjeze ine chakumwa!”

53 Chabwino, ife sitikanatha kuchita zimenezo. Ine ndinati, “Ine sindingathe kukuwonjezera chisoni ku zisoni zako. Ine ndikufuna kuti ndikuthandize iwe.”

54 Mbiri yake yonse. Iye anabwera kunyumba, usiku wina, ndipo apo panali, chimene iye anachitcha, kalata ya “Wokonedwa John” pa—pa tebulo. Nthawi imeneyo, mkazi wake anali atamuchokera iye. Ndipo anali. . . Iye ankamukonda iye. Ndipo iye anali atatenga ana ake. Ndipo iye anasudzulidwa, ndipo mkaziyo anali atathawitsana ndi mwamuna wina. Ndipo iye anati, “Ine sindinadziwe choti nkuchita, kuti chitontholetse ubongo wanga, kapena choti ndichite. Chotero ine—ine ndinatsikira ku bala.” Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, pamenepe iye anali. Izo ziri konsekonse pa dziko.

55 Wabodza. Inu mukhoza kumutenga mmodzi, monga ine ndinanena kwa mwamuna, tsiku lina, amene ine ndinkaganiza kuti ankanena nthabwala. Ndipo ndinadzapeza, kuti, iye ananena mabodza ambiri mpaka iye amawakhulupirira iwo kwenikweni, iyemwini. Ndipo ine ndinati, “Chimakupangitsa iwe uzichita zimenezo ndi chiyani?” Ndipo ine ndinakhala panso kuti ndiyankhulane naye iye. Ine ndinati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe. Nkhani zimenezo ndi zovuta kwambiri kuti anthu azikhulupirire.”

56 Iye anati, “Loyamba limene ine ndingakumbukire kulinena.” Iye anati, “Ine ndinali mnyamata wamng’ono amene ndinaleredwa mu nyumba yabwino.” Ndipo iye anati, “Ine ndinapita panja ndipo ndinakasuta ndudu za nyenje za chimanga, basi kuti ndingokhala dolo. Ndipo ine ndinakadya khofi wina, kuti ndichotse izo mu mpweya wanga.” Ndipo iye anati, “Ine ndinakachitira izo kuseri kwa chotulutsira utsi chakale, kuseri kwa nyumba.” Ndipo iye anati, “Ine sindidzaiwala konse, pamene amayi anandigwira ine, ndipo ananena kwa ine, ‘Mwana, undilole ine ndinunkhize mpweya wako.’ Ndipo ine ndinapemelera mpweya wanga pa nkhope yawo, ndipo iwo anati, ‘Iwe wadya khofi kuti uchoitse chinachake mu mpweya wako. Kodi iwe wakhala ukuchita chiyani? Kodi iwe wakhala ukusuta ndudu?’”

57 Ndipo iye anati, “Chinachake chimandiuza ine kuti ndiwauze iwo zoono.” Iye anati, “Koma ine ndinati, ‘Ay, amayi. Ine ndikulumbira. Ine sindimasuta ndudu.’” Iye anati, “Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, zimenezo zinayambitsa izo.”

58 Ife tonse tikhoza kupeza chinachake chimene—chimene chinayambira pa nthawi inayake. Ndipo kuyambira pamenepe mpakana, zinthu zinasintha. Ndipo pali zinthu zina zoyenera zimene ife tikhoza kuziganizira. Amuna a zolinga zabwino ayeserapo kuyamba zinthu mwatsopano, kuti achite zinthu pa nthawi inayake.

<sup>59</sup> Mwa chitsanzo, pamene magetsi anapangidwa koyamba ndi Benjamin Franklin, ndipo iwo anakwanitsa kuwapeza iwo. Iwo anayamba kunena kuti, “Kuyambira nthawi ino mpakana, sikudzakhalanso nkondo. Chifukwa, chakuti, magetsi awa akhoza kuikidwa mmipanda, ndi mphamvu yamagetsi yaikulu imeneyo, mpaka kuti palibe munthu amene angadzadumphe.” Iwo ankatanthauza zabwino.

<sup>60</sup> Ndipo itangotha Nkhondo Yoyamba Yadziko lonse, pamene—pamene Kaiser Wilhelm anasaina mgwirizano wa mtendere. Ife tinauzidwa kuno mu Amerika. Ine ndinali mnyamata wa pafupifupi usinkhu wa zaka naini zakubadwa. Koma ine ndikutha kukumbukira za anthu onse akuti, “Ife sitidzakhalsano ndi nkondo ina. Kuyambira nthawi ino mpakana, iyo yatha, mpaka kalekale.” Koma ife tinali nayo nkondo ina.

<sup>61</sup> Ndipo pamene U.N. yaikulu. Kapena, ine ndikhoza kunena kuti, pambuyo pa iyo, iwo anali ndi chimene chinkatchedwa League of Nation. Ndipo iwo anati, “Tsopano ife sitimakhalanso ndi nkondo, chifukwa ife tiri ndi League of Nations imene iziyang’anira dziko. Ndipo pakakhala kuukirana kwinakwake, amuna awa kuchokera ku fuko lililonse azipita kumeneko ndi kukaliyang’anira dzikolo.” Koma izo zinali zolephera. Iwo anapitirirabe kumakakhala ndi nkondo. Ndipo U.N. ikhala chinthu chomwecho.

<sup>62</sup> Ife tauzidwa tsopano mwa kuneneratu kuti mawa usiku kapena Lamlungu usiku... Munthu yemwe uja amene ananeneratu za Pearl Harbor, molondola nthawi yeniyeni imene nde—ndege zikanadzaphulitsa iyo, wanena, kuti, “Lamlungu usiku pa thwelofu koloko, kuti sevente-faifi peresenti ya anthu Achimerika adzakhala phulusa, kuti Russia adzaphulitsa United States, usiku wa Lamlungu likubwerali thwelofu koloko.” Munthu yemwe uja amene ananeneratu za Pearl Harbor. Iwo sakuziika izo poyera, chifukwa anthu abalalika. Ine sindikuzikhulupirira. Mukuona? Ayi. Chifukwa, ilo silingazunzike ndi nkondo ya atomiki. Imodzi yawo idzadutsa kupyola chotchinga zomvekazo, mbali *iyi*, ife tidzawaponyera iwo mbali *iyi*, ndipo dziko lidzakhala zidutswa. Chinachake chiyenera kuti chichitika, apobe, Yesu asanabwere. Uko nkulondola.

<sup>63</sup> Mwa chitsanzo, anthu awiri okwatirana kumene. Inalipo nthawi ina imene iwo anali atangokwatirana. Ndipo iwo—iwo anaika malumbiriro awo pamodzi. Ndipo analonjezana, wina kwa mzake, kukhulupirika kwawo. Ndipo iwo ananena, kuti, “Ife tidzakondana, kulemekezana ndi kusamalirana wina ndi mzake, bola ngati tonse tiri moyo.” Koma inadzafika nthawi imene chinachake chinadzachitika.

<sup>64</sup> Zinthu zonse izi, pamakhala—pamakhala nthawi imene chinachake chinachitika. Ndipo mwinamwake malumbiriro awo onse, ndi ma league of nations onse, ndi zina zotero, mwinamwake anali ndi cholinga chabwino, koma zonsezo zimafika pamathero. Zonse zikusweka, pansi pa—pa—pa phazi la munthu. Ndi zolinga zabwino zonse zimene ife tikhoza kukhala nazo, koma zonse ziyenera kudzafika pamathero.

<sup>65</sup> Koma ilipo nthawi imene munthu akhoza kufika ku chinachake chimene chiri Chamuyaya. Pamene ndi pamene, munthu, nthawi imene munthu akumana ndi Mulungu. Apo ndi pamene chinachake chimadzachitika chimene chimakhala Chamuyaya.

<sup>66</sup> Ife timapanga kulakwitsa kwathu. Ndipo timapanga malumbiriro athu pa usiku wa Chaka Chatsopano, nkudzangowaswa iwo tsiku lotsatiralo. Ife timatsegula masamba atsopano, ndipo ife timaika malumbiriro. Ndipo ife timapita kwa ansembe ndiku... Ife sititero, koma Akatolika amatero. Ndipo amakalapako, ndi kusaina malonjezo, ndipo timabwera pa guwa ndi kudzatsegula masamba atsopano, koma zonsezo pachabe. Pakuti, nthawi ina winawake akatipalamula kapena chinachake, mkwiyo wakale uja umabwereranso. Nthawi iliyonse imene ife tikhala pavuto kapena chinachake, izo zimadzachitikanso.

<sup>67</sup> Koma pali malo amene munthu akhoza kubwera, pa nthawi, amene angamusinthe iye mpaka kalekale, kwa Muyaya. “Iye amene azadza kwa Ine, Ine sindidzamtaya iye mwanjira iliyonse,” anatero Yesu. Munthu akhoza kubwera kwa Mulungu, ndipo kofikira kwake konse Kwamuyaya nkusintha. Ndipo munthu akhoza kukumana ndi Mulungu, ndipo iye osakhalanso chimodzimidzi konse. Iwe sungathe kukumana ndi Mulungu nkukhalabe munthu yemweyo amene iwe unali. Ngati iwe upotoloka kuthawa kwa Iye, iwe udzakhala munthu woipitsitsa kuposa mmene iwe unaliri. Ngati iwe umulandira Iye, iwe wapeza Moyo Wamuyaya, ndipo Iye adzakuukitsa iwe pa tsiku lomaliza, mwa lonjezo Lake.

<sup>68</sup> Panali nthawi imene panali munthu wotchedwa Abrahamu, amene anabwera kuchokera ku Alkadea, ndipo iye ankakhala mu mzinda wa Ur. Ndipo iye anangokhala munthu basi, munthu wabwino. Mwina, mwinamwake iye anali... Abambo ake mwina ankapembedza mafano, chifukwa iwo anachokera ku Babeloni. Ndipo iye anali munthu wamba, ndipo iye amakalamba. Iye anali sevente-faifi, ndipo mkazi wake anali sikisite-faifi.

<sup>69</sup> Ndipo Abrahamu, tsiku lina, pamene iye mwinamwake anali kumunda, akusaka kapena chirichonse chimene iye anali kuchita, kutola nthuza, kapena chirichonse chimene ntchito yake inali, iye anakumana ndi Mulungu. Ndipo kuyambira

nthawi imeneyo, iye anasinthika. Iye ankatha kuzitcha zinthu zimene panalibepo, ngati kuti izo zinalipo, chifukwa iye anali atakumana ndi Mulungu. Iye anali akudziwa miniti ndi ora imene iye anakumana ndi Mulungu. Izo zinamusintha iye. Ndipo Mulungu anamuitana iye kuti adzakhale atate a mafuko ambiri. Ndipo amakhulupirira Mulungu ndipo amakhulupirira lonjezo Lake, chifukwa iye anali atakumana ndi Mulungu. Zaka twente-faifi mtsogolo, iwo anali akukambirana, kuyesera kuti amunyoze iye, kumuza iye kuti anali atakhulupirira chinachake chimene chinali cholakwika. Koma Baibulo linati, “Iye ankakhala wamphamvu nthawi zonse, akupereka matamando kwa Mulungu.” Chifukwa, iye ankadziwa kuti Mulungu amayenera kusunga lonjezolo.

<sup>70</sup> Apo ndi pamene munthu amakumana ndi Mulungu. Izo zimamusintha mapangidwe ake. Izo zimamupatsa iye mphamvu yapamwamba. Monga ine ndimayankhulira usiku wina, munthu wachibadwa amakhala ndi mphamvu zisanu basi. Koma, wokhulupirira, pamene iye akumana ndi Mulungu, iye amapeza chinachake chosiyana. Icho ndi mphamvu yapamwamba imene imamukwezera iye mmwamba pamwamba pa mithunzi. Iyo imamupangitsa iye kukhulupirira zinthu zimene zimakhala zosatheka kuti zingachitike. Iye amakhulupirirabe kuti izo zichitika, chifukwa Mulungu wanena chomwecho. Pamene munthu akumana ndi Mulungu, chinachake chimachitika.

<sup>71</sup> Inalipo nthawi imene munthu anali ataphunzitsidwa mu nzeru zonse, fioloje yonse ya Mawu a Mulungu. Iye ankawadziwa Iwo mwa lemba. Iye anali ataphunzitsidwa. Iye anali ndi madigrii onse. Iye anali wophunzira kwambiri mpaka iye amatha kuwaphunzitsa ophunzira achi Igupto ndi aziphunzitsi awo. Iye ankazidziwa zonsezo, mwa lemba. Koma wamantha ndi izo, amene ankathawathawa, anapita kuseri kwa chipululu ndipo anali kuweta nkhosa za mlendo. Koma inadzafika nthawi imene Mulungu anakumana naye kumeneko, mu chitsamba chonyeka moto. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, Mose anasinthika, chifukwa iye anakumana ndi Mulungu mu chitsamba chonyeka. Ndipo maso ndi maso ndi Mulungu, iye sakanakhalanso chimodzimidzi.

<sup>72</sup> Pamene mwamuna kapena mkazi . . . Ine sindikusamala kaya ndi malumbiriro angati amene inu mupanga, kapena ndi masamba atsopano angati amene inu mutembenuza. Mpaka inu mutadzakumana ndi Mulungu, inu simungathe kusinthidwa. Koma pamene inu mukumana ndi Mulungu kamodzi, zikatero inu mumasinthika mpaka kalekale.

<sup>73</sup> Sizinangomusintha Mose yekha. Izo zinasintha Israeli. Izo zinasintha Igupto. Izo zinalisintha dziko pa nthawi imeneyo, chifukwa munthu mmodzi anakumana ndi Mulungu ndipo anamutenga Iye pa Mawu Ake.

<sup>74</sup> Chimene ife tikuchisowa lero ndi winawake kuti akumane ndi Mulungu, maso ndi maso, ndi kuyankhulana Naye, chochitikacho. Pamene anthu akumana ndi Mulungu, zinthu zimasintha. Ndithudi. Iyo ndi njira yokhayo imene ife tingakhale ndi zinthu.

<sup>75</sup> Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, Mose wamantha, Mose amene ankathawa, anasinthidwa. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye anadzakhala wantchito wa Mulungu. Izo nthawizonse zimagwira ntchito mwanjira imeneyo. Pamene munthu akumana ndi Mulungu, zinthu zimasintha.

<sup>76</sup> Panali mtsikana wamng'ono nthawi ina, wosapitirira usinkhu wa zaka eyitini zakubadwa, kapena mwinamwake osati wamkulu monga choncho, amene anali panjira yake akupita ku chitsime mmawa wina, kuti akatunge chidebe cha madzi, uko mu Nazareti. Iye anali mtsikana wabwino wamng'ono. Iye ankahulupirira. Iye anali ndi chikhulupiriro. Koma, mmawa umenewo, iye anakumana ndi Mulungu. Ndipo Mulungu anamuuza iye chinachake, ndipo iye anakhulupirira izo. Ndipo icho chinasintha machitidwe onse a moyo wa mkaziyo, ndipo chinamupanga iye wachisavundi. Dzina lake linali Maria, amake a Ambuye Yesu wathu. Dona wamng'onoyo anangokhala basi mtsikana wamng'ono wawamba, koma iye anakumana ndi Mulungu. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo mpakana, chinachake chinachitika. Ndithudi.

<sup>77</sup> Panali munthu dzina lake Petro, nsodzi wokalamba wolimba, mwinamwake wankhanza basi mmene iwo amadzera. Ndipo iye mwinamwake anali chiphanza chachikulu. Chifukwa, kuno nthawiina kale, ine ndinawonera seweru, lotchedwa, “Nsodzi Wamkulu.” Ine ndinaganiza kuti uko kunali kufotokoza kwabwino kwa Petro, chifukwa iye anali munthu wamkulu wolimba. Iye samasamala kalikonse. Iye samakhulupirira nkomwe chirichonse. Koma, tsiku lina, iye anakumana ndi Mulungu. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye anasinthika. Kuyambira nthawi imeneyo, iye anadzakhala mtumwi wa Ambuye Yesu Khristu.

<sup>78</sup> Monga M'bale David duPlessis amatiuza ife kanthawi kapitako, za Saulo waku Tariso, wakupha, amene amagwirizira chikhothi cha okupha, icho, ndipo anachitira umboni, ndipo anapereka umboni ku imfa ya Stefano woferayo. Iye anali ndi makalata mmatumba mwake, kuti apite uko—malikulu a mipingo, ndi kukawamanga anthu amene amapanga phokoso lambiri, kufuula, ndi kupembedza Mulungu. Iye anali munthu wamkulu pamaso pa Afarisi. Iye anali Mfarisi wa Afarisi. Koma, tsiku lina, iye anali panjira yake waku Damasiko, ndipo iye anakumana ndi Mulungu. Kuwala kunawala momuzungulira iye. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye sanalinso Sauli waku Tariso. Koma iye anakhala Paulo, wodzichepetsayo,

wofatsayo, chifukwa iye anakumana ndi Mulungu, ndipo Izo zinamusintha iye.

<sup>79</sup> Kunali wakhate atagona pa chipata. Njira zonse za mankhwala sizimakhoza kumuchiza iye. Mabala ake onunkha anali atakula mpaka amakanika kukweza manja ake mmwamba, kenanso. Ndipo mapazi ake, iye amalephera ngakhale kuwasuntha iwo. Nkhani yake inali yopanda chiyembekezo. Koma iye anakumana ndi Mulungu, tsiku lina, akubwera akutuluka pa chipata. Ndipo iye anagwa pansi ndipo anampembedza, ndipo anati, “Ngati Inu mungafune, Inu mukhoza kundiyeretsa ine.”

<sup>80</sup> Ndipo Iye anati, “Ine nditero. Iwe khala woyera.” Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye sanakhalenso ndi khate, chifukwa iye anakumana ndi Mulungu.

<sup>81</sup> Kunali munthu wakhungu amene ankakhala pambali pa msewu. Ndipo iye samatha kuwona kuwala kwa tsiku akakhala ku mdima. Panalibepo chirichonse chimene chikanamuthandiza iye. Tsiku lina, Winawake anabwera akuyenda akutuluka mu mzinda wa Yeriko, ndipo pamene iye anakumana ndi Mulungu; ndipo kuyambira nthawi imeneyo, iye amatha kupenya. Kupenya kwake kunabwera kwa iye. Kupenya kwa kuwala kunali kutatsegukira mmaso mwake, ndipo iye amatha kuwona aponso. Chifukwa, kuyambira nthawi imeneyo, pamene iye anadzakumana ndi Yesu, iye anadzakhala munthu wosiyana. Iye analandira kupenya kwake.

Pamene munthu akumana ndi Mulungu, chinachake chimachitika ndithudi.

<sup>82</sup> Kunali mnyamata, nthawi ina; mosakaika, mbadwa yabwino ya mdziko, koma khunyu linabwera pa iye. Ndipo iye anali moipa kwambiri mpaka nyumba ya ndende sinakhoze kumusunga iye. Ndipo iwo amamumanga iye ndi unyolo. Ndipo iye anali ndi chikhamu cha ziwanda, mwa iye, mpaka iye amatha kudula unyolo ndi kuzimasula yekha. Ndipo ziwanda zinamupititsa iye ku manda, kumene iye ankakhala kumeneko. Ndipo iye amanyamula mapale ndipo, amakhala wokwiya kwambiri, iye amakhoza kudzichekachekha yekha. Oh, iye anali munthu wowopsya. Pamene khunyu limenelo limuchokera iye, mosakaika iye amatha kuganiza, “Kodi ine ndikuchita chiyani kuno?” Ndipo pa nthawi imeneyo, ziwandazo zimabweranso kwa iye, ndi kudzamudula iye ndi kudzamung’amba iye. Koma, tsiku lina, iye anakumana ndi Yesu. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, wamisala waku Gadara anayamba kuganiza bwino, anavala, anayamba kuyenda ndi mapazi Ake. Iye anakwanitsa kubwerera kwawo, ngati njonda. Iye anakwanitsa kubwerera ku chitukuko. Iye anakwanitsa kubwerera kwa okonedwa ake, ndipo anatha kunena kuti, “Kuyambira nthawi ija, ine ndasinthidwa.” Inde.

<sup>83</sup> Linali tsiku lina, uko pa Kalvari, pamene Mulungu ndi imfa zinakumana, maso ndi maso, pamene Moyo ndi imfa zinabwera pamodzi. Koma pamenepo ndi pamene Moyo, Khristu, anachotsa mbola pa imfa. Ndipo kuyambira nthawi imeneyo, imfa ilibe mbola mwa iyo. Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izo. Mulungu! Imfa ndi Mulungu zinakumana, pamodzi. Imfa siinakhalebe chimodzimidzi. Iyo ilibe mbola pa iyo tsopano. Wokhulupirira wa Chikhristu akhoza kufika pamaso pake ndikuti, “O imfa, mbola yako ilikuti? Manda, chigonjetso chako chirikuti?” Bwanji? Iwo onse anakumana ndi Mulungu. Iwo siali chimodzimidzi kuyambira pamenepo.

<sup>84</sup> Palibe munthu amene angakhale chimodzimidzi, palibe kanthu kamene kangakhale chimodzimidzi, pamene kakumana ndi Mulungu kamodzi. Inu simudzakhalanso chimodzimidzi.

<sup>85</sup> Ine ndikukhoza kukumbukira nditagona kuno pa bedi laku chipatala. Madokotala atandipatsa ine maminiti atatu akukhala moyo. Mtima wanga ukugunda, ka seventini pa miniti. Ine ndinakumana ndi Mulungu. Kuyambira nthawi imeneyo, ine sindinakhaleenso chimodzimidzi. Chinachake chinandichitikira ine. Palibe amene akanandiuza ine kusiyana kulikonse. Bill Branham anamwalira. Ine ndinakumana ndi Mulungu, ndipo Chinachake chinabwera mwa ine. Ine sindinakhaleenso chimodzimidzi kuyambira miniti imeneyo imene ine ndinadzakumana naye Iye. Iye anandisinthina ine. Iye anandipanga ine chinachake chosiyana. Ichu sichinali kutenga lumbiro la Chaka Chatsopano, koma ine ndinakumana ndi Mulungu.

<sup>86</sup> Amuna ndi akazi, pamene inu mukumana ndi Mulungu, inu mumasinthika. Ife tipanga malumbiro athu a Chaka Chatsopano usikuuno; tikabwerera mawa mmawa, tikawaswa iwo; tsiku lotsatira, tikawaswa iwo. Koma chimene ife tikuyenera kuchita, si lumbiro la Chaka Chatsopano, koma ife tikusowa kubwera maso ndi maso ndi Mulungu, ndi kukhala nawo Moyo Wamuyaya, kubadwa mwa Mzimu Wake.

<sup>87</sup> Kunali bambo wokalamba, nthawi ina, ndipo iye samatha kupanga chiganizo. Mdierekezi anapitiriza kumumenya iye chifukwa cha izo. Tsiku lina, ali ku munda, iye anagwada pansi kuti apemphere. Pamene iye anali kupemphera, iye anakhomera pansi chikhomo. Iye anati, “Ichi chikhale chikumbutso. Satana, ngati iwe udzabwere konse kwa ine kenanso, ine ndidzakulozera iwe ku chikhomo ichi. Ndipo ine ndidzakuuza iwe kuti pomwe pano ine ndinakumana ndi Mulungu, ndipo izo zinakonzedwa kuyambira pano.” Ndicho chimene ife tikusowa, mwinamwake osati chikhomo mmunda, koma kwina kwake, malo enaake obisika, malo enaake. Osati a . . .

<sup>88</sup> Oh, usikuuno, pakhala mazana a malumbiro ati atengedwe, zikwi za iwo atengedwa. Ndipo chaka cha mawa ife tidzayenera



kuti tidzawatengenso onse, kenanso. Ife tidzati, “Ife tisiya kunama. Ife tisiya kuchita *izi*. Ndipo ife tisiya kumbali mkwiyo wathu. Ife tichita zochuluka za Mulungu. Ife tichita *ichi*, kapena *icho*, kapena *chinacho*,” kudzangopeza kuti, izo ndi pachabe.

<sup>89</sup> Koma chimene munthu akusowa kuti achite, usikuuno, ndi kubwera maso ndi maso ndi Mulungu. Ndipo kuyambira pamenepo, iye akhala cholengedwa chosinthika. Aleluya! Oh, ine ndikukhumba ndikanazinena izo mmene ine ndikuzikhulupirira izo. Koma pamene munthu wakumana ndi Mulungu, iye amakhala wosinthika, kuyambira miniti imeneyo, masiku ake onse. Iye sadzakhhalanso chimodzimodzi, chifukwa iye ali nawo Moyo Wamuyaya. Iye ndi cholengedwa chatsopano. Zinthu zakale zapita, ndipo zinthu zonse zasanduka zatsopano kwa iye. Iye akuwoneka watsopano.

<sup>90</sup> Munthu wodwala akhoza kupita pamaso pa Mulungu, pamene madokotala anena kuti, “Iye afa.” Koma iye akhoza kupita pamaso pa Mulungu, ndi kukachondelera mlandu wake. Ndipo iye nkuchokako, ali munthu wosinthika, ndipo kuyambira nthawi imeneyo.

<sup>91</sup> Oh, ine ndikukumbukira Congressman Upshaw, atakhala mu chikuku kwa zaka sikisite-sikisi. Usiku uja, uko mu California, pamene Mzimu Woyera unatsika, ndi kuyamba kuyankhula, iye anakumana naye Mulungu. Ndipo kuyambira pamenepo, iye amakhoza kuyenda wopanda ndodo zake.

<sup>92</sup> Ine ndawonapo nthawi zimene anthu odyedwa ndi khansa atagona, opanda kalikonse koma mthunzi. Ndipo madokotala amadutsapo ndikuti, “Iwo afa.” Okonedwa awo nkusonkhana, kuti anene mawu awo omaliza amene iwo angathe, kwa iwo, achimbikitso. Koma iwo anakumana ndi Mulungu, ndipo, kuyambira nthawi imeneyo, iwo anasinthika. Iwo akukhala mosinthika.

<sup>93</sup> Ine ndikutha kumuwona mkazi woipa, uko pa msewu. Ine ndikutha kumuwona chidakhwa, uko mngalande. Ine ndikutha kumuwona wachinyengo, uko mu tchalitchi. Anthu osiyanasiyana onsewo, Chaka Chatsopano chirichonse, akutembenuza tsamba latsopano, ndipo akuyesetsa kuti achite chinachake chosiyana, kuyesetsa kuti akakonze ndi kuchita zina zotero. Mungowasiya iwo akumane ndi Mulungu, nthawi ina, ndipo kuyambira pamenepo.

<sup>94</sup> Yesu analalikira kwa iwo kuyambira nthawi imeneyo, amene ankakhala mmadera a mthunzi wa imfa.

<sup>95</sup> Ndipo ine ndikuti, usikuuno, ngati munthu akufuna kuti akhale ndi kusintha kwenikweni kutabwera pa iye, musiyeni iye abwere maso ndi maso ndi Mulungu, ndipo akumane naye Iye kamodzi, akatero iye akhoza kunena kuti, “Kuyambira pamenepo, kuyambira nthawi imeneyo, ine

ndinadzakhala munthu wosinthika. Ine ndikudziwa pachimene chinandichitikira.”

<sup>96</sup> Mu kanthawi pang’ono, mpingo ukhala ukusonkhana pano kuzungulira guwali. Inu mukhala mukuyeretsa miyoyo yanu, mwatsopano. Inu mukhala mukusiya zinthu, ndi kuziyika zinthu pa guwa. M’bale, ndiloleni ine ndikupatseni inu malangizo ena. Ngati inu simunayambe mwakumanapo ndi Mulungu, maso ndi maso, ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Inu mukhale pa guwa limenelo. Mungokhala pamenepo mpaka inu mutakumana ndi Mulungu, mukatero inu mukhoza kudzalozza chala chanu ku usiku wa Chaka Chatsopano umenewo. Osati, ndikuti, “Ine ndinatembenuza tsamba latsopano. Ine ndinapanga lonjezo latsopano.” Koma, “Kuyambira nthawi imeneyo, ine ndinakumana ndi Mulungu. Ndipo moyo unasinthika, ndipo zinthu zinasintha. Ndipo chirichonse chinakhala chatsopano, kwa ine, kenanso, kuyambira nthawi imeneyo,” nthawi imene inu mukumana ndi Mulungu.

<sup>97</sup> Izo si, kukumana ndi Chaka Chatsopano. Ife tikumana nacho icho, mu maminiti pang’ono. Pakapita kanthawi, pafupifupi maora awiri ndi theka, ine ndikuganiza. Mwinamwake kuchepera kuposa pamenepo. Ife tikhala tikukumana ndi Chaka Chatsopano, maso ndi maso. Ife tikumana nacho icho ndi malumbiriro. Ife tikumana nacho ndi malonjezo. Ife tikumana nacho ndi cholinga chabwino. Ife tikumana nacho, tikuti, “Ife tiyesera kutembenuza tsamba latsopano. Ife tiyesera kuchita mosiyana.” Zonsezo ndi zabwino. Ine ndikuyamikira zimenezo.

<sup>98</sup> Koma m’bale, izo sizingakhale za Muyaya mpaka inu mutakumana ndi Mulungu, poyamba. Pamene inu mukumana ndi Mulungu, koyamba, ndipo, kuyambira pamenepo, chirichonse chidzakhala chosinthika.

Tiyeni tipemphere pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>99</sup> Ambuye Yesu, Mwana wa Mulungu, ine ndikukumbukira nthawi imene ine ndinakumana ndi Inu, Ambuye. Ine ndikukumbukira, munthu womvetsa chisoni, kumakhala moyo wa makhalidwe abwino, osati woyendayenda, kumwa, kapena kuchita juga, kapena kusuta, kapena zina zotero. Koma ine ndinadziwa, Ambuye, pamene imfa inadzabwera kudzakwawira mchipinda cha chipatala chija, zaka twente zapitazo, panali chinachake chimapelewerwa mmoyo mwanga. Kumeneko ine ndinakumana ndi Mulungu, ndipo kuyambira nthawi imeneyo. Kuyambira nthawi imeneyo, Ambuye, ine ndayesetsa kukutumikirani Inu. Moyo wanga wasinthika ndipo chirichonse chikuwoneka chosinthika. Ndine wokondwa kwambiri kuti ndinakumana ndi Inu, Ambuye. Ndipo usikuuno, ndikuyang’anizana ndi Chaka Chatsopano, ndine wokondwa kunena kuti ine ndikhoza kuyang’anizana nacho ndiri ndi Mzimu wa Mulungu wa moyo mu mtima mwanga.

<sup>100</sup> Tipatseni ife zotichitikira, Ambuye. Tipatseni ife za ubwino Wanu ndi chifundo. Tikhulukireni ife machimo athu. Ndipo mutilole ife tikhale kudutsa chaka chikubwerachi, O Ambuye Mulungu, ndi chotichitikira, kuti ife takumana nanu Inu ndipo miyoyo yathu yasinthika. Perekani izi, Ambuye. Tikhulukireni ife zolephera zathu. Muike mkati mwathu Mzimu Woyera Wanu. Mutitsogolele ife ndi kutilondolera ife.

<sup>101</sup> Atate, Mulungu, apa pali 1960, ikundiyang'ana ine. Ndipo pali mimwayi ya msonkhano wa dziko lonse, kumene zikuwoneka ngati ngakhale mateni a masauzande kuchulukitsa masauzande, ndi masauzande ndi masauzande achikunja enieni, a osapembedza, ndi ena otero, akhoza kubwera kwa Inu. O Ambuye Mulungu, ndi Mzimu Wanu mu mtima mwanga, ine ndikuyang'anizana ndi guwa Lanu, usikuuno, ndi kuyang'anizana ndi Inu, ndikuti, "Ndithandizeni ine, O Mulungu. Mtima wanga ukutentha ndi changu. Ine ndimakukondani Inu, Ambuye. Ine ndikudzipereka ndekha kwa Inu, mu utumiki. Nditsogolereni ine kulikonse kumene Inu mukufuna kuti munditsogolere ine. Nditumizeni ine kulikonse kumene Inu mukufuna kuti munditume ine, Ambuye. Mungoyankhula, ndipo ine ndipita."

<sup>102</sup> Mudalitse mpingo wanga. Mumudalitse M'bale Neville. Muwadalitse anthu onse pano, alendo mu zipata zathu. Ndi azibusa awa amene akhale akuyankhula, mosinthana nthawi, kudutsa utikuwu, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudalitse utumiki wawo. Mumudalitse M'bale Neville. Mumudalitse M'bale Junie Jackson. M'bale Beeler, atumiki ena onse awa, adalitseni iwo, Atate. Tipatseni ife chaka chopambana mu 1960.

<sup>103</sup> Ife, Ambuye, amene tikudziwa kuti takumana ndi Inu, maso ndi maso, ndipo tikudziwa chimene chikutanthauza kubadwa mwatsopano mwa Mzimu Wanu, tipatseni ife za chisomo Chanu Chamuyaya, kuti tikakutumikireni Inu. Mu Dzina la Yesu ife tikupemphera. Ameni.

<sup>104</sup> Inu mukumukonda Iye? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] 1960, musalole izo zikhale, kuti, "Ine ndinatembenuza tsamba latsopano." Musalole izo zikhale, kuti, "Ine ndikuyesera kuyamba moyo watsopano." Koma mulole izo zikhale, kuti, "Ine ndinakumana ndi Mulungu, ndipo kuyambira nthawi imeneyo, nthawi imeneyo mpakana, ine ndinakhala ndi mtendere umene umadutsa kumvetisa. Ine ndinakhala ndi chimwemwe chosaneneka, ndi chozadza ndi ulemelero. Ine ndinakhala ndi kukhutitsidwa. Ngakhale ngati imfa itabwera kwa ine, ine ndidzakhala ndiri mmanja a Mulungu, miniti nditatsiriza kupuma mpweya wanga wotsiriza. Ziribe kanthu kuti kukubwera chiyani kapena chikupita!"

<sup>105</sup> Asiyeni iwo aliphulitse ilo, Lamlungu usiku, ngati iwo akufuna kutero. Iwo akufuna kutero, bombalo lisanatsirize kung'aluka ife tidzakhala tiri mu Ulemelero ndi Iye. Amen. Palibe chinthu chimene chingativulaze ife. Aleluya!

<sup>106</sup> Ndine wokondwa kwambiri kuti ine ndinakumana ndi Mulungu. Ndine wokondwa kwambiri ndikhoza kunena kuti, "Kuyambira nthawi imeneyo." Kuzikhomerera izo pansi pa malo amenewo! "Pamene ine ndinakumana ndi Mulungu, chinachake chinadzachitika kwa ine. Ine ndinasinthika, kuyambira miniti imeneyo. Ine ndinasinthika, kuyambira pamenepo." Ndine wokondwa kwambiri kuti ndiri pa njira iyi, usikuuno, ngati umboni ku Ulemelero ndi Mphamvu ya Mulungu. Chinachake chakale chaching'ono kunja kuno, ndipo Mulungu anadzatsika pamenepo ndipo anandipatsa ine chisomo Chake, ndipo anandipulumutsa ine, ndipo anandichiritsa ine, ndipo anandizadza ine ndi Mzimu Wake. Ndipo ndiloleni ine ndilalikire Uthenga Wake, chimene chiri ulemu waukulu umene ulipo mdziko. Kuyambira nthawi imeneyo, mpaka nthawi ino, ine sindinakhalepo ndi kudandaula kumodzi. Koma ine ndakhala wothokoza, masiku onsewa, ndipo ine ndidzakhala, kudutsa Umuyaya wonse, kuti ine ndinakumana ndi Mulungu.

Mulungu akudalitseni inu. Chabwino, M'bale Neville.



*NDIPO KUYAMBIRA NTHAWI IMENEYO* CHA59-1231  
(And From That Time)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, unalalikidwa mu Chingerezi, Usiku Wolowa Chaka Chatsopano, Lachinai usiku, Disembala 31, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2019 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)